



UNDUNA WA ZACHILENGEDWE
Nthambi Yoona za Nyengo ndi Kusintha kwa Nyengo

ULOSI WA KAGWEDWE KA MVULA M'DZINJA LA 2026 – 2027


CHIRADZULU DISTRICT

Mwachidule

Nyengo ya dzinja ya 2026-2027 ikuyembekezeka kukhudzidwa ndi El Nino wa mphamvu. El Nino ndi kutentha kopyola muyezo kwa madzi m'dera la pakati chakum'mawa kwa nyanja yamchere ya Pacific zomwe zimakhudza kagwedwe ka mvula dziko lonse.

Boma la Chiradzulu likuyembekezeka kulandira mvula ya **mulingo wokhazikika kapena kuchepera apo** mu nyengo ya dzinja ya 2026/2027.


October 2026



Madera ambiri ayembekezere nyengo yotentha ndi mvula ya mlingo yosapitilira 30mm.

Mphenzi ndi mphepo yamkuntho ikuyembekezerekanso m'mweziwu.


November 2026



Mu mwezi wa November, madera ambiri m'bomali akuyembekezereka kudzalandira mvula yamlingo wapakati pa 50mm ndi 100mm.


Mvulayi idzabwera yamabingu ndi mphepo yamkuntho.

December 2026




Mvula yamlingo woposera mlingo okhazikika ndi mlingo wapakati pa 200mm ndi 250 mm ikuyembekezereka kudzagwa m'madera ambiri. Mvula yokhazikika ikuyembekezereka kudzayamba sabata lachiwiri lamwezi wa December.

January 2027



Mwezi wa January ukuyembekezereka kudzakhala ndi mvula yochepera mlingo okhazikika m'bomali. Madera ambiri adzalandira mvula ya mlingo wochepera 200mm Pali chiopsyezo cha ng'amba ya sabata imodzi.


February 2027



Boma la Chiradzulu likuyembekezereka kudzalandira mvula yamlingo wochepera mlingo okhazikika kuchokera 50mm kufikira 100mm.

Pali kuthekera kwa ng'amba ya masabata awiri mu mwezi wa February.


March 2027



Madera ambiri akuyembekezereka kudzalandira mvula ya mlingo wa 150-200mm. Pali kuthekera kwa mvula yoposera 200mm kwa T.A Likoswe ndi T.A Nkalo.

Nyengo ya dzinja ikuyembekereka kupita kumapeto sabata lomaliza la mwezi wa March.

April 2027



Mu mwezi wa April madera ambiri akuyembekezereka kudzalandira mvula ya mlingo wapafupifupi 50mm.

DZINJA MWACHIDULE

Kuyamba kwa mvula yokhazikika

Ikuyembekezereka sabata lachiwiri mu December 2026

Ng'amba

Ng'amba ya sabata imodzi mu mwezi wa January komanso sabata ziwiri mwezi ya February


Kutalika kwa nyengo yadzinja

Dzinja lidzakhala masiku apakati pa 100 ndi 120

Mathero a mvula dzinja

Sabata lomaliza la mwezi wa March

MONTH	NORMAL RANGE	FORECAST
OCT	1.1	21.5
NOV	10.5	67.4
DEC	71.1	171.3
JAN	130.2	236.2
FEB	96.8	170.2
MAR	72.8	174.4
APR	19.0	106.3



Zasindikizidwa ndi thandizo lochokera ku:



Tsatilani ulosi ndi malangizo ochokera ku nthambi yoona zanyengo



For further information contact:

The Director of Climate Change and Meteorological Services,
P.O. Box 1808, Blantyre.



+265 991 69 00 61



metdept@metmalawi.gov.mw



www.metmalawi.gov.mw